

Elected councillor - Dinde Ward

SOCIAL CONTRACT AGREEMENT

BETWEEN

PARTIES"

CONSTITUENCY: Nsanje South West Constituency
CANDIDATE NAME DUMBA GEORGE MARY
I, Dumba this day 23 of month APRIL year 2014

Make agreement with people of Nsanje South West Constituency that if voted as a Ward Councillor for Dinde Ward during the tripartite elections on 20th May, 2014, I DO hereby solemnly promise THAT I shall do in accordance with what contained herein my manifesto during my term of office given the necessary conditions.

I, George Mark Dumba

Contact Details 0834471201 Signature George

Witnessed by Five Signature

Title COUNCILLOR

Constituency Nsanje South West (Dinde Ward)


Date 23/04/2014

As Name; MALEMA Signature Malema

Witnessed by Five Signature APR 2014

Constituency NSANJE SOUTH WEST

Date 23/04/2014



This Agreement has been sealed AND SIGNED by ME on the behalf of the electorates of Nsanje South West Constituency this day of 2/5/14

BEFORE ME [Signature] Commissioner of Oaths Private Bag 1, Nsanje COMMISSIONER FOR OATHS

SHADOW COUNCILOR FOR DPP MR DUMBA MARK GEORGE

MFUNDO ZIKULU ZIKULU ZOMWE ANGADZATSATIRE POFUNA KUTUKULA ANTHU PA CHITUKUKO MU DERA LINO LA DINDE WARD ATASANKHIDWA **PA 20 MAY 2014 PANO.**

NTCHITO YOMWE NDIDZAGWIRE MUKADZANDISANKHA

INE NGATI MASO ABOMA KUMUDZI KOMANSO MULEMBI WA ASSEMBULE NDI WOYIMILIRA ANTHU AKUMIDZI PA NKHANI YA CHITUKUKO KUDERA LINO LA DINDE WARD NDIDZAONETSETSA KUTI ZITUKUKO ZIKUYENDA MOYENERA NDIKUPINDULIRA ANTHU AKUDERA LANGA .

CHŪMA CHABOMA CHODZIWIKA BWINO KUPINDULIRA ANTHU KUMADERA MONGA ICHI!!!

- CONSITUENCY DEVELOPMENT FUND (CDF)
- LOCAL DEVELOPMENT FUND (LDF)
- DIRECT SUPPORT SCHOOL PROGRAME (DSSP)

1. CHITUKUKO CHA MADZI

- INE NDIDZAONETSETSA KUTI MALO OMWE MADZI AKUVUTA KAMBA KOSOWA MIJIGO NDIDZAKHAZIKITSEKO MIJIGO
- NDIDZAYESETSA KUPANGITSA MAPHUNZILO MAKOMITI AMIJIGO MUDERA YANGA PANKHANI YA KAYANG'ANILIDWE NDIKASAMALIDWE KA MIJIGO POFUNA KUPEREKA MPHAMVU KUANTHU.
- NDIDZATHANSO KUUNIKIRA MABUNGWE PA MALO OMWE ALI NDI VUTO LA MADZI MUNO MU DINDE WARD.

2. NKHANI YA MAPHUNZIRO

- NDIDZAONETSETSA KUTI MA SUKULU A NKOMBA PHALA AKHAZIKITSIDWA MALO OYENERA KOMANSO APHUNZITSI AKE AKUSAMALILIDWA MOYENERA.
- NDIDZIDZAPANGITSA MISONKHANO YOLIMBIKITSA MAKOLO KULIMBIKITSA ANA ACHITSIKANA KUPITANSO KU SUKULU NGATI ANASIYA CHIFUKWA CHOPATSIDWA MIMBA ALI PA SUKULU KOMANSO NDI ANA ONSE.
- KUONETSETSA KUTI SCHOOL MANAGEMENT COMMITTEE IKUGWILITSA BWINO NDI MOYENERA NDALAMA ZA (DSSP) POKONZETSELA ZOFUNIKA PA SUKULU.

3. NKHANI YA ULIMI

- NDIDZAONETSETSA NDIKULIMBIKITSA ALIMI KUKHALA MMAGULU OMWE MABUNGWE AKUFUNA KWABWINO ADZIDZATHA KUWAPEZA MOSAVUTA NDIKUWAPHUNZITSA ZA ULIMI WA MAKONO NDI MOMWE ANGAMAPEZERE MISIKA YA ZOKOLOLA ZAWO KUTI MLIMI APINDULE KU MBEWU ZAKE.
- NDIDZAYESETSA KUDZANENELERA ULIMI WA NTHILIRA KU MABUNGWE AKUFUNA KWABWINO MONGA KU MALO AWA ;
 - ✓ DINDE
 - ✓ MBANGU
 - ✓ LAMBWE NDI NKOTAMU

4. NKHANI YA UMOYO

- NDIDZAONETSETSA KUTI ZIPATALA ZA ANA AANG'ONO ANG'ONO ZILI NDI MA HSA's NDIPO AKUGWILA NTCHITO NDI ANTHU AKUMUDZI MOYENERA NDI MWANSANGALA.
- NDIDZANENELERA MA CLINIC KU ASSEMBULE KUTI AAMANGILE KOMANSO KUWALIMBIKITSA ANTHU KUUMBA NJERWA ZOGWIRITSILA NTCHITO.
- NDIDZAONETSETSA KUTI ASSEMBULE YAKHAZIKITSA MALO OTAYIRA ZINYALALA MU MISIKA YONSE NDI KUMANGA ZIMBUDZI .

5. NKHANI YA ZA MASEWERO

- NDIDZANENELERA KWA MP KUTI ADZAKHAZIKITSE CHIKHO CHA MPILA WA MIYENDO NDI WA MANJA MU CONSITUENCY MUNO YA SW
- NDIDZAGULILA ANA A KU MASUKULU A NKOMBA PHALA MIPILA YOSEWERELA MMASUKULU MWAWO.

6. NKHANI YA MISEWU

- NDIDZAONETSETSA KUTI ANTHU OMWE AKULEMBEDWA MISEWU YA MASAFU NDIOYENERADI KOMANSO AKULEMBANA MWA WINA ALIYENSE OSATI OKHAOKHAWO NTHAWI ZONSE.
- NDIDZAONETSETSA KUTI BOMA IDZAYANG'ANENSO MMENE ANGASAMALIRE NSEWU OCHOKA KU CHIDIDI KUPITA.KU LURWE.
- NDIDZAONETSETSA KUTI MISEWU YA MASAFU NDI INA YAING'ONOING'ONO ILI NDI MILATHO YOLIMBA.
- NDIDZAONETSETSANSO KUTI MA CONTRACTOR OMWE AKUPATSIDWA NTCHITO YOMANGAMANGA AKHALE OVOMEREZEKA OSATI ANTHU OSADZIWA NTCHITO YAWO.

7. NKHANI YA CHITETEZO

- NDIDZAONETSETSA KUTI A POLISI AKUMUDZI ALI PAUBALE WABWINO NDI ANTHU AKUMUDZI NDI A POLICE POFUNA KUSAPEREKA MPATA KWA ANTHU AKUBA NG'OMBE NDI ZINTHU ZINA.
- NDIDZAPEMPHANSO MALO NGATI KU CHIDIDI KUYENDEREDWA NDI A POLICE KAWILI PAABATA POFUNA KUPELEKA CHITETEZO.

NOTE : ZINTHU ZONSEZI ZIDZATHEKA NGATI MUNGADZANDISANKHE PA 20 MAY 2014 !!!